**SPEECH**

**BY**

**HIS EXCELLENCY**

**DR. LAZARUS MCCARTHY CHAKWERA,**

**PRESIDENT OF THE REPUBLIC OF MALAWI**

**AND PRESIDENT OF**

**MALAWI CONGRESS PARTY**

**AT**

**THE LAUNCH OF THE MALAWI CONGRESS PARTY**

**2025-2030 MANIFESTO**

**BINGU NATIONAL STADIUM**

**LILONGWE, MALAWI**

**19TH APRIL 2025**

**Amayi ndi Abambo,**

**Anyamata ndi Asungwana,**

**AMalawi nonse komwe muli,**

**Mau anga oyamba lero ndi okuthokozani. Mmwezi wa June chaka cha 2020, anthu osachepera 2.6 million mdziko muno munandipatsa voti yanu kuti ndikutumikileni ngati Pulezidenti. Ndine othokoza koposa kuti Mulungu anakupatsani chikhulupiliro kuti munditume ntchito yokutsogolerani, ntchito yomwe sindinakaikwanitsa olo chaka chimodzi popanda chisomo cha Mulungu komanso sapoti yanu.**

**Kwa aMalawi 50,277 omwe munandivotela ku Chitipa, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 32,706 omwe munandivotela ku Chikwawa, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 11,777 omwe munandivotela ku Chiradzulu, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 74,665 omwe munandivotela ku Karonga, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 18,108 omwe munandivotela ku Balaka, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 170,268 omwe munandivotela ku**

**Dedza, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 235,972 omwe munandivotela ku Dowa, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 13,631 omwe munandivotela ku Thyolo, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 46,610 omwe munandivotela ku Zomba, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 9,456 omwe munandivotela ku Mwanza, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 135,181 omwe munandivotela ku Mchinji, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 33,293 omwe munandivotela ku Mangochi, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 88,985 omwe munandivotela ku Ntchisi, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 6,092 omwe munandivotela ku Phalombe, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 14,983 omwe munandivotela ku Machinga, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 199,421 omwe munandivotela ku Kasungu, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 77,439 omwe munandivotela ku Nkhotakota, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 2,981 omwe munandivotela ku Likoma Island, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 6,652 omwe munandivotela ku Neno, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 45,591 omwe munandivotela ku Nkhatabay, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 21,923 omwe munandivotela ku Nsanje, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 81,914 omwe munandivotela ku Ntcheu, ndikuti**

**zikomo. Kwa aMalawi 77,977 omwe munandivotela ku Salima, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 17,499 omwe munandivotela ku Mulanje, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 55,153 omwe munandivotela ku Rumphi, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 142,911 omwe munandivotela ku Blantyre, ndikuti zikomo. Kwa aMalawi 287,488 omwe munandivotera ku Mzimba, ndikuti zikomo. Komanso kwa inu aMalawi 644,730 amene munandivotela kuno ku Lilongwe, ndikuti zikomo. Zikomo, zikomo, zikomo.**

**Tsiku lomwe nonsenu munandivotela lija, tinanyamuka limodzi pa ulendo omanga Malawi watsopano. Ndipo ulendo umeneu tayenda zaka zokwana fayifi tsopano, ndipo muulendo umene tikuyendela limodziu, takumana ndi zinthu zosiyanasiyana, zina zokoma chifukwa cha ntchito yomwe tagwira limodzi pomanga zitukuko mmaboma onse, zina zowawa zimene sitinayembekezere kuti zitichitikira tiri mnjira. Zinthu zowawazo ndiye nzosayamba, chifukwa titangoyenda miyezi sikisi paulendo wathuwu, ndipaja tinagunda khoma la Covid, dziko lonse maliro, ntchito kuima, mabizinesi**

**kusokonekela. Titayendanso kufika chaka cha 2022, tinachitanso ngozi ya mphepo ya Cyclone Ana ndi Gombe, yomwe inasakaza minda, zakudya, katundu, ndi miyoyo. Chaka chomwecho ndichija feteleza ndi mafuta anakwera mtengo koopsya dziko lonse lapansi chifukwa cha nkhondo ya Russia ndi Ukraine, kutisokonezela ma plan opeza ndi kugulitsa feteleza motchipha. Titayendanso kufika 2023, ndipaja tinapanga ngozi ziwiri, mliri wa cholera omwe unapha anthu mmaboma onse, komanso Cyclone Freddy yomwe inasokoneza miyoyo ya anthu oposa 2 million. Titayendanso kuchoka apo tinapanganso ngozi ya ng'amba ya El Nino, yomwe inanyalitsa theka ya chakudya mdziko muno nkubweretsa njala pa miyoyo ya anthu oposa 5 million. Kuchoka pamenepo ndipaja chaka chathachi tinagwedwanso ngozi ya ndege yomwe inatenga moyo wa malemu a Vice President Dr. Saulos Chilima ndi anthu ena 8. Ndiye ngozi zomwe takumana nazo mnjira yaulendo wathu ngati aMalawi ndizowawa, ndipo lero ndikufuna ndithokoze Mulungu wakumwamba kuti muzowawa zonsezi sanatisiye amasiye. Kupanda inu aMalawi, kulimbikira kwanu pantchito, kupilira kwanu**

**pa ululu omwe takumana nawo, komanso kusunga mtendere ndi bata, sibwezi lero dzikoli liri lolozeka.**

**Koma chifukwa chachikhulupiliro chanu, mwalimbana nako kulimbana kwabwino, ndipo ndikuthokozeni kuti ngakhale pa mudzi sipamalephera kupezeka ena otaya mtima ndi chiyembekezo, ambiri a inu amene munandivotela mmaboma onse 28, mwakhala mukundipanga sapoti komanso kundipemphelera. Ambuye akudalitseni aliyense wa inu. Sapoti yanu ndi imene yandithandiza kuti ndikwaniritse zitukuko zomwe zafika mmaboma anu. Sapoti yanu ndi imene yandithandiza kuti tikwanitse kupereka ndalama 250 billion za NEEF kwa mabanja 275,000. Sapoti yanu ndi imene yandithandiza kuti tikwanitse kupereka mtukula pakhomo kwa ma banja oposa 300,000 dziko lonse. Sapoti yanu ndi imene yandithandiza kuti tisinthe miseu ndi nkhope ya mzinda wa Lilongwe. Sapoti yanu ndi imene yandithandiza kuti tiyambe kukonze nseu wa M1, nseu wa M5, ndi miseu ina. Kulikonse kumene muliko mMalawi muno, ngati wakumana ndi chigalimoto chikulima nseu m'boma lanu, pamenepo mudziwe kuti**

**manja anga afikapo olo nkhope yanga musaione, chifukwa ntchito yokonza miseuyo tikuikwanitsa chifukwa cha sapoti yanu. Sapoti yanunso ndi imene yandithandiza kudzutsa njanji ndi mastima mdziko muno. Sapoti yanu ndi imene yandithandiza kukonza ubale wathu ndimaiko ena, omwe akhala akutithandiza munthawi yangozi komanso omwe apanga commit ndalama zomwe titamangire nseu wa Makanjira ku Mangochi, Judicial Complex kuno ku Lilongwe, ndi zitukuko zina. Sapoti yanu ndi imene yandithandiza kuti pa achinyamata 6 million amene mumasowa zi ntchito, 2 million tawapezera zintchito mzaka fayifi zimenezi. Sapoti yanu ndi imene yandithandiza kuti aziphunzitsi, apolisi, asilikali, ma nesi, ndi ma civil servant ambiri akwezedwe pantchito komanso akwezeredwe malipiro. Sapoti yanu ndi imene yandithandiza kuti alimi afodya, asoya, achimanga, anandolo, azigulitsa zolima zawo pamtengo wabwino. Sapoti yanu ndi imene yandithandiza kuti chiwerengero cha anthu omwe amalandira feteleza wa subsidy chichoke pa less than 1 million chifike more than 3 million. Sapoti yanu ndi imene yandithandiza kuti achinyamata a secondary school tiwamangire ma school atsopano oposa 200,**

**komanso kupereka ma bursary kwa oposa 40,000. Sapoti yanu ndi imene yandithandiza kuti nambala ya ma University student opeza ma loan ichoke pa 10,000 idutse 30,000. Sapoti yanu ndi imene yandithandiza kuti chiwerengero cha anthu okhala nyumba ya magetsi chikwere kuchoka 11% kufika 25%. Sapoti yanu ndi imene yandithandiza kuti tikhwimitse chitetezo nkuthetsa mchitidwe opha abale athu achialubino. Sapoti yanu ndi imene yandithandiza kuti anthu am'boma omwe akuyankha mulandu wa ziphuphu ndiziwachotsa pampando olo atakhala kuti ndi nduna. Sapoti yanu ndi imene yandithandiza kuti timange ma Health Post 200, komanso timange ma District Hospital, ma Border Post, ma Biriji, ma Police Unit, ma Stadium, ma District Council Office, manyumba anthu achitetezo, National Cancer Center, komanso ma facility atsopano mma University athu. Sapoti yanu ndi imene yandithandiza kuti tibweretse ma tractor ambiri omwe alimi athu akugwiritsa ntchito pokhazikitsa ma mega farm. Sapoti yanu ndi imene yandithandiza kuti tisunga umodzi yamitundu yathu.**

**Ndikudziwa kuti nthawi yonena zonse zimene tachita limodzi mzaka fayifi zimenezi ndiyosakwana, koma kwakukulu ndimangoti ndikuthokozeni chifukwa cha sapoti yanu. Komanso ndikudziwa kuti ziripo zina zomwe ndinanena kuti ndichita koma sinnakwanitse chifukwa cha ngozi ndi mavuto ena omwe tinakumana nawo paulendo wathu, koma popeza malamulo amampatsa Pulezidenti mpata okhala m'boma zaka 10 kuti amalize ntchito yake, ndi chifukwa chake ndikukupemphaninso kuti mundilole kupitiliza ntchito yomwe munandipatsa kuti tipititse chitukuko chathu patsogolo.**

**Ndiye zomwe ndakonzeka kuchita mzaka fayifi zikubwerazi ndizimene ndaika mManifesto imene ndatsekula panoi. Pa maziko fayifi a Hi-5 omwe takhala tikumanga mzaka fayifi zapitazi, tiyambano kumangapo nsanamira fayifi zotukula miyoyo yanu kuti ipite patsogolo. Nsanamira yoyamba mManifesto imenei ndi Food Security, kapena kuti Chakudya Chofikira Aliyense, ndipo ndakonza ma programu ndi ma project abwino omwe cholinga chake nkuonetsetsa kuti pofika**

**2030, tikhale dziko lodzidyetsa lokha ndipo njala ija tikhale titathana nayo. Nsanamira yachiwiri mManifesto imenei ndi Job Creation, kapena kuti Ntchito Zokwanira Aliyense, ndipo mmenemu ndaika mfundo zolembera ntchito achinyamata okwa 3 million mzaka fayifi zikubwerazi. Nsanamira yachitatu mManifesto imenei ndi Wealth Creation, kapena kuti Kuchulukitsa Chuma Chanu, ndipo mmenemu ndaika mfundo zoti tichulukitse zikhwaya mdziko muno, mwa chitsanzo program yosandutsa NEEF kukhala banki yothandiza achinyamata ndi amayi kupeza mpamba wa bizinesi yotentha, komanso muli program ya Ten-Ten Challenge, yomwe itasankhe achinyamata ndi azimayi 10,000 omwe atapatsidwe mpamba wa 10 million kwacha aliyense nkuthandizidwa kupanga bizinesi ya siriyasi. Nsanamira yachinayi mManifesto imeneyi ndi Governance Reform, kapena kuti Kuyendetsa Boma Mwamakono, ndipo mmenemu ndaika ma plan angapo, monga plan yanga yothetsa udindo wa ma city CEO nkuyambitsa zisankho za ma Meya amizinda kuti muzisankha nokha aMalawi kuti ma Meya muziwapatsa mphamvu yotukula mizinda yathu kukhala yamakono. Komanso muli plan yoti mu Cabinet yanga, muzakhala**

**achinyamata osachepera 4 azaka zochepera 35 kuti achinyamata mukhale mkati mwenimweni mwaboma kuyendetsa nawo zones. Komanso muli mfundo yopanga restructure Office of the President and Cabinet kuti kukhale anthu othamangitsa zinthu ndi ma digital system, osati kumachedwetsa zinthu ndi ma system akalekale. Nsanamira yotsiriza mManifesto imenei ndi Public Service Delivery, kapena kuti Kulimbikitsa Ubwino Waboma, ndipo ndaikamo Chakwera Masterplan, yomwe itakupatseni ma service atsopano okwana 72 mma sector okwana 24, ndicholinga kuti pofika 2030, muzamve kuti mukukhala mdziko lomwe liri ndi chikhalidwe chonyadilitsa, chuma chodalirika, komanso maufulu otetezedwa. Ma service 72 amenewa muli mfundo ngati ntchito yoyika ma flushing toilet mmizinda yonse, mmisika yonse, ma community secondary school onse, ndi ma health facility onse. Mulinso mfundo zotsekula tsogolo account ya mwana aliyense obadwa kuti timupangire invest deposit ya 500,000 kwacha mpaka azafike zaka 18 kuti m'badwo umeneu ukhale oyamba mMalawi opanda mphawi olo mmodzi. Mulinso mfundo zoika ma program othandiza makolo kulandira training pa nkhani za mental health**

**kuti akhale ndikuthekera kothandiza achinyamata amene akuvutika ndi mental health mmanyumbamu. Mfundo zonse 72 ndaziyala mmenemu kuti tipititse chitukuko chanu patsogolo.**

**Ndiye ndikuthokozeni inu a Hon. Henry Mumba, a MCP Director of Economic Planning, ndi timu yanu yonse amene munakhala nane pansi kuphika chimanifesto chabwino komanso chokongola ngati chimenechi. Komanso inu a Hon. Moses Kunkuyu, a MCP Director of Campaigns, mutenge manifesto imenei muonetsetse kuti onse amene akupanga nawo kampeni yanga chaka chino aziwafotokozera aMalawi mfundo zomwe ziri mManifesto imenei. Koma chachikuru nchoti ineyo ndikudzipereka kwa inu aMalawi kuti mundilore kuyenda nanu ulendo omwe tinauyamba mu 2020, chifukwa maziko omwe taika mzaka fayifi zimenezi ndiolimba ndipa mukandikhulupiliranso zaka fayifi zina, musimba okoma ndithu mtsogolomu.**

**In a special way, I want to thank our development partners for coming to this Manifesto Launch, and I want**

**to thank captains of Industry and Private Sector players for gracing this occasion. I can assure you that you will find in this Manifesto the best blueprint for our partnership in taking the development of Malawi forward, so as we have worked together for the past five years, I look forward to working with you in the next five years. Also in a special way, I want to thank all members of Malawi Congress Party for trusting me to be your presidential candidate again in this election, and I want to thank you for registering in large numbers to ensure that we have a commanding victory on September 16. I promise to campaign harder than anyone because come September 16, I will make sure that you are part of the winning team.**

**Ine ndili ndichikhulupiliro kuti pamene Mulungu anandiika pa mpando umeneu, anali nafe cholinga ngati dziko, ndipo ndili ndichikhulupiliro kuti cholingacho chikhala chitakwaniritsidwa pofika 2030, chifukwa umboni wa ntchito yamanja anga uli mmaboma onse mdziko muno, ndipo kwangotsala zaka fayifi zokha kuti ubwino wantchito zomwe ndikupanga umfikire aliyense.**

**Manifesto ndi yomweyi ndithu ndipo boma lake lokutumikirani ndilomweli.**

**Ambuye akudalitseni nonse. Zikomo.**